-Anthu amenewa amakhulupilira mwa Yesu Mpulumutsi.
-Anthu amenewa amakhulupilira M'mawu a Mulungu, ndipo amabereketsa zipatso zambiri.

-Kodi mtima wanu uli ngati nthaka yabwino?



# PHUNZIRO LA 55

1. Kodi chifukwa chiyani Afarisi anamuda kwambiri Yesu?
-Chifukwa chakuti Yesu anaŵawuza kuti Iye ndi Mulungu Mpulumutsi.

2. Kodi chifukwa china chimene Afarisi anankamudera Yesu chinali chotani?
-Chifukwa chakuti Yesu anaŵawuza kuti iwo ndi ochimwa, ndipo Mulungu adzaŵalanga ngati satembenuka mitima.

3. Kodi chifukwa china chimene Afarisi anankamudera Yesu chinali chotani?
-Chifukwa chakuti anthu ambiri ankamutsata Yesu, Afarisi ankamuchitira kaduka Iye.

4. Kodi Yesu anakakhala kuti waswa lamulo limodzi mwa malamulo a Mulungu, Afarisi anakachita chiyani?
-Anakamulamula kuti aphedwe.

5. Kodi chifukwa chiyani Yesu sanaŵamvere Afarisi?
-Chifukwa chakuti Afarisi anaŵasintha malamulo a Mulungu.

6. Kodi Afarisi anaŵasintha bwanji malamulo a Mulungu?
-Anawonjezera malamulo awo pa malamulo a Mulungu, ndikuŵapangitsa kuti akhale abodza.

7. Kodi chifukwa chiyani Yesu anakwiya kwambiri ndi Afarisi?

-Chifukwa chakuti anayiwona kuti mitima yawo inali yowuma kwambiri.

8. Kodi Yesu anadziŵa bwanji kuti mitima yawo inali yowuma kwambiri?
-Yesu akhoza kuwona mu mtima mwa munthu wina aliyense.
-Yesu amawudziŵa mtima wa munthu wina aliyense.

9. Kodi Afarisi anachita chiyani Yesu atamuchiza munthu opuwala dzanja uja?
-Afarisi anaturuka mu sunagoge muja ndi kuyamba kupanga upo wa m'mene angamuphere Yesu.

10. Kodi chifukwa chiyani ziwanda zinamutcha Yesu kuti ndi Mwana wa Mulungu?
-Chifukwa chakuti zinadziŵa kuti Yesu anachokera kwa Mulungu Atate.

11. Kodi chifukwa chiyani ziwanda sizifuna kuti inu muzikhulupilira mwa Yesu.
-Ziwanda sizifuna kuti inu mudzikhulupilira Yesu chifukwa chakuti sizikufuna kuti inu mupulumuke ku mphamvu yawo.

12. Mwa anthu amene anamutsatira Yesu, kodi Iye anasankha anthu angati kuti akhale ophunzira ache?
-Khumi ndi aŵiri.

13. Kodi anthu khumi ndi aŵiri ameneŵa ankatchedwa kuti ndani?.
-Alariki.



Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:20

20-"Anthu ena ali ngati njere zogwera pa nthaka yabwino, amamva Mawu a Mulungu, amaŵalandira, ndipo amabala zipatso zopindula makumi atatu, ndi makumi asanu ndi limodzi, ndi makumi khumi.

-Kodi nthaka yabwino imakhala bwanji?
-Ndi nthaka imene imakhala italimidwa bwino.

-Kodi mulimi akadzala mbewu mu nthaka yabwino, ingabereke zipatso?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti nthakayo siyolimba.
-Chifukwa chakuti nthakayo ndiyakuya.
-Chifukwa chakuti nthakayo ilibe minga.
-Chifukwa chakuti nthakayo yalimidwa bwino.

-Kodi anthu amene ali ngati nthaka yabwino ndi ati?
-Anthu ameneŵa amati akamva Mawu a Mulungu, amafikira kuŵakhulupilira, ndikubereketsa zipatso zambiri.

-Anthu ameneŵa amadziŵa kuti abadwira mu tchimo.

-Anthu ameneŵa amadziŵa kuti tchimo lawo likuyenera kulandira chilango cha imfa yosantha.

-Anthu ameneŵa amadziŵa kuti Mulungu yekha ndi amene angathe kuŵapulumutsa.

-Kodi nthaka imene ili ndi minga yambiri imakhala bwanji?
-Imakhala nthaka imene siyinalimidwe.

-Kodi mulimi akadzala mbewu mu nthaka ya minga yambiri, ingabereke zipatso?
-Ayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti mingazo zitsamwitsa mbewuzo.

-Yesu analankhulanso kuti mitima ya anthu ena ili ngati nthaka ya minga.

-Kodi anthu amene ali ngati nthaka ya minga ndi ati?
-Anthu ameneŵa amalankhula kuti akukhulupilira mwa Mulungu, koma zofuna zawo zimakhala zofunika kwambiri kwa iwo kuposa Mulungu.

-Anthu ameneŵa amalankhula kuti akukhulupilira mwa Mulungu, koma kukhala ndi ndalama zambiri ndi kofunika kwambiri kwa iwo kuposa Mulungu.

-Anthu ameneŵa amalankhula kuti akukhulupilira mwa Mulungu, koma kukhala ndi nyumba yayikulu kapena ng'ombe zambiri ndikofunika kwambiri kwa iwowo kuposa Mulungu.

-Kodi mtima wanu uli ngati nthaka ya minga yambiri?

-Yesu ananenanso kuti mitima ya anthu ena ili ngati nthaka yambwino.



-Yesu atatha kusankha ophunzira ache khumi ndi aŵiri aja, anapitiriza kuphunzitsa anthu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:1

1-Ndipo Yesu anayambanso kuphunzitsa pambali pa nyanja. Ndipo khamu lalikuru linasonkhana kwa Iye, kotero kuti Iye analoŵa mu ngalaŵa nakhala m'nyanja, pamene khamu lonse linakhala pa mtunda m'mbali mwa nyanja.

-Chifukwa cha khamu lalikuru la anthu, Yesu anakhala mu ngalaŵa m'nyanja pamene khamu lonse linakhala pa mtunda m'mbali mwa njanja ndi kumamvera chiphunzitso chake.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:2a

2a-Ndipo Yesu anaŵaphunzitsa zinthu zambiri m'mafanizo

-Yesu ankaŵaphunzitsa anthu m'mafanizo.

-Kodi fanizo ndi chiyani?
-Fanizo ndi nkhani imene imaphunzitsa zowona zenizeni za Malungu kwa anthu amene akufuna kumvetsetsa.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anayamba kuŵaphunzitsa anthu m'mafanizo?
-Ngakhale kuti anthu ambiri ankamutsata Yesu, iwo sankamukhulupilira.

-Ngakhale kuti anthu ambiri ankamutsata Yesu, iwo sankachikhulupilira chiphunzitso chache.

-Anthu ambiri ankamutsata Yesu kuti adzimuwonera Iye akuchiza anthu, koma sankakhulupilira mu chiphunzitso chache.

-Anthu ambiri ankamutsata Yesu kuti adzimuwonera akutulutsa ziwanda mwa anthu, koma sankakhulupilira mu chiphunzitso chache.

-Chifukwa chakuti anthu sankakhulupilira mu chiphunzitso chache, Yesu anayamba kuŵaphunzitsa anthu m'mafanizo.

-Pamene Yesu ankaphunzitsa, anaŵaphunzitsa anthu fanizo la munthu ofesa mbewu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:2b-12

2b-Ndipo m'chiphunzitso chache [Yesu] anati:
3-"Mverani! Mlimi anapita kukafesa njere zache.
4-Ndipo akufesa njerezo, zina zinagwera m'mbali mwa njira, ndipo mbalame zinabwera ndikudzadya njerezo.
5-Njere zina zinagwera pa nthaka ya tanthwe, pamene panalibe nthaka yambiri. Ndipo pomwepo zinamera mosavuta chifukwa chakuti panalibe nthaka yakuya.
6-Ndipo dzuŵa litakwera, zinafota, kenako zinapserera chifukwa chakuti zinalibe mizu.
7-Njere zina zinagwera pa minga, ndipo mingazo zitakula, zinatsamwitsa mbewuzo ndipo



-Kodi anthu amene ali ngati nthaka ya pa tanthwe ndi ati?
-Pakamwa pawo ndi zochitika zawo amawoneka ngati amakhulupilira mwa Mulungu, koma m'mitima mwawo mulibe chikhulupiliro china chilichonse.

-Anthu ameneŵa amalankhula kuti akukhulupilira, koma mavuto akafikira amasiya kukhulupilila mwa Mulungu.

-Anthu ameneŵa amalankhula kuti akukhulupilira mwa Mulungu, koma anthu ena akafika ndi zinthu zina kwa iwo, amasiya kukhulupilira mwa Mulungu.

-Anthu ameneŵa amalankhula kuti akukhulupilira mwa Mulungu, koma akayamba kuziwopa ziwanda, amasiya kukhulupilira mwa Mulungu.

-Kodi mtima wanu uli ngati nthaka ya pa tanthwe?

-Yesu ananenanso kuti anthu ena ali ngati nthaka imene ili ndi minga yambiri.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:18-19

18-"Anthu ena ali ngati njere zogwera pa minga, amamva mawu a Mulungu;
19-koma madandawulo a moyo uno ndi chinyengo cha chuma ndi zilakolako pa zinthu zina zimadza ndikutsamwitsa mawu, ndipo amaŵapangitsa kukhala opanda chipatso."

Mulunguwo kuchokera kwa iwo.

-Kodi mtima wanu uli ngati njira?

-Yesu anatinso kuti mitima ya anthu ena ili ngati nthaka ya pa tanthwe.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:16-17

16-"Anthu ena ali ngati njere zogwera pa tanthwe, amati akamva mawu a Mulungu amaŵalandila nthaŵi yomweyo mosangalala.
17-Koma chifukwa chakuti alibe mizu, amangokhala kwa kanthaŵi kochepa. Mavuto kapena mazunzo akadza chifukwa cha zinthu za pa dziko, amagwa mwansangansanga.

-Kodi nthaka ya pa tanthwe imakhala bwanji?
-Ndi nthaka yosaya.

-Kodi chifukwa chiyani siyikhala yakuya?
-Chifukwa chakuti pasi pake pamakhala tanthwe.

-Kodi mulimi akadzala mbewu yache pa nthaka ya pa tanthwe, ibereka zipatso?
-Ayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti nthakayo siyakuya, ndipo mizu yache siyingapite pasi kwambiri.

-Yesu ananena kuti mitima ya anthu ena ili ngati nthaka ya pa tanthwe.



sizinabare zipatso.
8-Komabe njere zina zinagwera pa nthaka yachonde. Zinamera ndipo zinabala zipatso ndikukula ndikuchuluka; ndipo zinabala kupindula makumi atatu, ndi makumi asanu ndi limodzi mpaka makumi khumi.
9-Kenako Yesu anati, "Amene ali nawo makutu omvera , amve."
10-Ndipo pamene Yesu anali payekha, iwo amene anali pafupi ndi Iye pamodzi ndi ophunzira ache khumu ndi aŵiriwo anamufunsa Iye za mafanizowo.
11-Ndipo Iye anati kwa iwo, "Chinsinsi cha ufumu wa Mulungu chaperekedwa kwa inu. Koma kwa onse amene ali kunja zonse zinenedwa m'mafanizo
12-kuti kupenya apenye koma asazindikire, ndipo kumva amve koma asamvetsetse: kuti mwina mwache angatembenuke ndi kukhululukidwa.

-Kwa anthu amene sankamukhulupilira Yesu, sanalimvetse kose fanizo limeneli.

-Koma kwa anthu amene ankamukhulupilira Yesu, analimvetsa bwino bwino fanizo limeneli ndipo anaphunzira zambiri za Mulungu.

-Mulungu adzakuphunzitsani inu pokhapokha ngati mukufuna kuchidziŵa chowona chenicheni.

-Ngati simukufuna kuchidziŵa chowona chenicheni, Mulungu sadzakuphunzitsani.

-Ophunzira a Yesu atafunsa za tanthawuzo la fanizo limeneli, izi ndi zimene ananena Yesu:

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:13-14

13-Kenako Yesu anati kwa iwo, Kodi simukulimvetsa konse fanizo ili? Nanga muŵamvetsa bwanji mafanizo ena onse?

14-Ofesa, afesa mawu.

-Kodi mu fanizoli, mbewu ndi chiyani?
-Mbewu ndi Mawu a Mulungu.

-Kodi mu fanizoli, ofesa mbewu ndi ndani?
-Ofesa mbewu ndi munthu amene akulalikira Mawu a Mulungu.

-Yesu ananena kuti, ngati m'mene palili nthaka ya mitundu itatu yofesamo mbewu, chomchonso pali mitima ya mitundu itatu imene Mawu a Mulungu amadzalidwamo.

-Yesu ananena kuti mitima ya anthu ena ili ngati njira.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:15

15-"Anthu ena ali ngati njere zimene zinagwera m'mbali mwa njira zija. Akangomva mawu a Mulungu, Satana amabwera ndikudzatenga mawu onse amene afesedwa mwa iwowo."

-Kodi nthaka ya m'njira imakhala bwanji?
-Imakhala yolimba kwambiri.

-Kodi chifukwa chiyani imakhala yolimba kwambiri?
-Chifukwa chakuti anthu ambiri amayendapo



-Kodi mulimi atadzala mbewu yache pa nthaka yolimba ya m'njira, mbewuyo ingabereke zipatso?
-Ayi.

-Chifukwa chiyani?
-Mbewuyo siyingaloŵe mu nthakamo chifukwa chakuti nthakayo ndi yolimba kwambiri.

-Kenako, mbalame ngakhale nyama zina zimabwera ndikudzadya mbewuzo.

-Yesu ananena kuti mitima ya anthu ena ili ngati njira yolimba.

-Kodi anthu amene ali ngati njira ndi ati?
-Anthu amene ali ndi mitima yolimba.

-Mawu a Mulungu sangadutse m'mitima yawo.

-Anthu ameneŵa safuna kumvera Mulungu.

-Anthu ameneŵa safuna kuti Mulungu aŵaphunzitse.

-Anthu ameneŵa safuna kutsatira Mulungu.

-Anthu ameneŵa amangofuna kutsatira njira za makolo awo.

-Anthu ameneŵa akamva Mawu a Mulungu, amaŵayiŵala nthaŵi yomweyo.

-Kenako Satana amabwera ndikudzatenga Mawu a